# PHUNZIRO LA 57

1. Kodi chifukwa chiyani Yesu anatopa?
-Ngakhale kuti Yesu anali Mulungu weniweni, Iye analinso munthu weniweni.

2. Kodi zinatheka bwanji kuti Yesu ayilamule mphepo ya nkuntho kuti isiye?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu.

3. Kodi chifukwa chiyani mphepo ndi nyanja zinamumvera Yesu?
-Chifukwa chakuti zinalengedwa ndi Yesu.

4. Kodi munthu ameneyu anakatha kudzipulumutsa yekha ku mphamvu ya ziwanda zimene zinkamulamulila iye?
-Ayi.

5. Kodi anthu ena anakatha kumupulumutsa iye ku mphamvu ya ziwanda zimene zinkamulamulila iye?
-Ayi.

6. Kodi tingadziŵe bwanji kuti ziwanda zimaŵada anthu?
-Chifukwa chakuti zinkamukakamiza muthuyo kumakhala ku manda.
-Chifukwa chakuti zinkamukakamiza munthuyo kuti adzi-dziduladula yekha pa thupi lache.

7. Kodi mfumu ya ziwanda zonse ndi ndani?
-Satana.

8. Kodi wamphamvu ndani kuposa satana ndi ziwanda zache?
-Mulungu.

9. Kodi chifukwa chiyani ziwanda sizinafe pamene nkhum-

ba zonse zinafa?
-Chifukwa chakuti ziwanda ndi mizimu.

10. Kodi amene anamupulumutsa munthu uja ku mphamvu ya ziwanda zija anali ndani?
-Yesu.
-Munthu uja sanalinso kapolo wa ziwanda.
-Munthu uja anamasulidwa ndi Yesu, Mpulumutsi.

-Tsiku lina Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anawombokera ku tsidya lina la nyanja ya Galileya.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:1-2

1-Pambuyo pake, Yesu anawomboka Nyanja ya Galileya (dzina like lina ndi Nyanja ya ku Tibeliya),
2-ndipo khamu lalikuru la anthu linamutsata Iye chifukwa chakuti anawona zizindikiro zambiri zozizwitsa zimene ankawonetsa pa anthu odwala.

-Kodi chifukwa chiyani khamu lalikuru kwambiri linamulondola Yesu?
-Chifukwa chakuti ankafuna kuti adziwona zizindikiro zambiri zozizwitsa zimene Yesu ankaŵachitira anthu odwala.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:3

3-Kenako Yesu anakwera pamwamba pa phiri ndikukhala pansi ndi ophunzira ache.

-Ngakhale kuti Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anapita ku phiri, khwimbi la anthu linamutsatilabe Iye.

-Khwimbilo linali lalikuru kwambiri, mwakuti chiŵerengero cheke chinakwana 5, 000.



34-Anthuwo anamupempha Yesu kuti, “Ambuye, muzitipatsa zakudyazi ife tsiku ndi tsiku.”

-Anthu sanamve.
-Ankaganiza kuti Yesu akulankhula za mkate wa matupi awo.

-Kodi Yesu ankalankhula za mkate wa matupi awo?
-Ayi.

-Yesu ankalankhula za mkate wa mzimu wawo.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:35

35-Yesu anaŵawuza kuti, “Ine ndi mkate umene umapereka moyo. Aliyense amene akubwera kwa Ine siyidzamukola njala, ndipo iye okhulupilira mwa Ine sadzamva ludzu.”

-Yesu analankhula kuti Iye ndi mkate wa uzimu ochokera kumwamba.

-Kodi wina akapanda kudya, adzafa?
-Inde.

-Ngati m’mene anthu angafere akapanda kudya, ifenso tidzafa ngati sitikukhulupilira mwa Yesu ngati chakudya cha mzimu wathu.

-Ngati tikukhulupilira mwa Yesu, mzimu wathu siwudzakhalanso ndi njala.

-Kodi Mose ankaŵapatsa mana a Isilayeli m'chipululu muja?
-Ayi.

-Kodi amene ankaŵapatsa mana a Isilayeli m'chipululu muja anali Ndani?
-Mulungu.

-Yesu anati kuti Mulungu Atate ndi amene ankaŵapatsa mana a Isilayeli m'chipululu muja.

-Yesu analankhulanso kuti, ngati m'mene Mulungu Atate ankaŵapatsila mana a Isilayeli m'chipululu muja, chomchonso Mulungu Atate ankaŵapatsa iwowo mkate weniweni kuchokera kumwamba.

-Kodi mkate weniweni umene Mulungu Atate anawupereka kuchokera kumwamba anali ndani?
-Yesu.

-Kodi Yesu anafanana bwanji ngati mana amene Mulungu Atate anapereka kwa a Isilayeli m'chipululu muja?
-Yesu anachokera kumwamba ngati m'mene anachokelera mana kumwamba.

-Yesu anaperekedwa ndi Mulungu ngati m'mene mana anaperekedweranso ndi Mulungu.

-Ngati m'mene a Isilayeli anakafera anakapanda kudya mana , chomchonso anthu adzafa ngati sakukhulupilira mwa Yesu.

-Kodi anthu anamva?

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:34



-Kenako Yesu anafunsa funso kwa m'modzi mwa ophunzira ache , Filipo,

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:5-7

5-Yesu atayang'ana mokweza maso ache, analiwona khamu lalikuru la anthu likubwera kwa Iye, ndipo anati kwa Filipi, "Kodi tngagule kuti mikate yakuti anthu ameneŵa ndikudya?"
6-Yesu anafunsa funso limeneli pofuna kungomuyesa Filipi, akudziŵa chimene achite m'maganizo ache.
7-Filipi anayankha kuti, "Ngakhale malipiro a miyezi isano ndi itatu sakukwanali kugula mikate yakuti aliyense adye!"

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anamufunsa Filipo funso limeneli?

-Yesu ankafuna kuti amuyese Filipo, ngakhale kuti Iye anadziŵa kale chimene ankafuna kuchichita.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:8-9

8-Ophunzira wache wina dzina lache Andileya, m'bale wache wa Simoni Petulo, anati kwa Iye,
9-"Pali mnyamata pano amene ali ndi mikate isano ya tiligu ndi msomba ziŵiri, kodi zimenezi zikwana bwanji kwa anthu ambiriŵa?

-Ophunzira a Yesu sankadziŵa za m'mene anakathera kudyetsa anthu onsewo.
-Apa pali zimene Yesu analankhula kwa iwo:

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:10-13

10-Koma Yesu anaŵawuza iwowo kuti, "Awuzeni

anthuwo kuti akhale pansi.” (pa malopo panali kapinga wambiri). Chomcho anthuwo anakhala pansi: Mu khamulo analipo anthu ngati amuna 5 000.

11-Yesu anayitenga mikate ija, ndipo anayamika kwa Mulungu, kaneko anaŵagayira mokwanira anthu amene anali pamenepowo. Yesu anachitanso chimodzimodzi ndi msomba zija, ndipo onse aja anaŵapatsa m’mene ankafunira.

12-Anthu onse aja atakhuta, Yesu anaŵawuza ophunzira che aja kuti, “Sonkhanitsani makombo otsalawo, tisataye chilichonse.”

13-Chomcho anasonkhanitsa makombowo ndipo anadzadza mitanga khumi ndi iŵiri ya mikate isano imene anaja anthu aja.

-Yesu atatha kuŵayamika Ambuye, anagaŵagaŵa mikateyo ndi msombazo, ndipo anazipereka kwa ophunzira ache kuti aŵapatse anthu.

-Kodi pamene Yesu ankayamba kuŵapatsa chakudya anthu, anali ndi mikate ndi msomba zingati?
-Mikate isano ndi msomba ziŵiri.

-Kodi Yesu anaŵadyetsa anthu angati ndi mikate isano ndi msomba ziŵiri?
-5 000.

-Kodi Yesu anatha bwanji kuŵadyetsa anthu 5 000 ndi mikate isanu ndi msomba ziŵiri?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Yesu akhoza kuchita china chilichose.

-Kodi anthuwo analankhula chiyani atatha kudya?

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:14-15



-Kodi yankho la Yesu linali lotani?
-Yesu anaŵayankha kuti ntchito imene iwo angayigwire kuti amusangalatse Mulungu ndi yokhulupilira mwa Iye basi.

-Kodi kenako anthu anazivomereza zimene ananena Yesu?
-Ayi.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:30-31

30-Iwo anamufunsa kuti, Kodi ndi chizindikiro chozizwitsa chotani chimene iwe ungachite kuti tichiwone kuti tikukhulupilire? Kodi uchita chiyani?

31-Makolo athu anadya mana m’chipululu, ngati m’mene malemba alembedwela kuti, “Iye wakupatsani mkate ochokera kumwamba kuti mudye.”

-Anthu analankhula kuti akufuna kuti Yesu adziŵapatsa mikate tsiku lililonso ngati m’mene Mose ankaŵapatsila mana a Isilayeli tsiku lililonse m’chipululu muja.

-Kodi Yesu anaŵayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:32-33

32-Yesu anati kuti, “Ndikukuwuzani inu zowona kuti, sanali Mose amene anakupatsani inu chakudya kuchokera kumwamba, koma Atate anga basi ndi amene amakupatsani inu chakudya chenicheni chochokera kumwamba.

33-Pakuti chakudya chimene amapereka Mulungu chili Iye amene amatsika pansi pano kuchokera kumwamba ndikupereka moyo weniweni kwa anthu a pa dziko lonse la pansi.”

-“Musagwire ntchito chifukwa cha chakudya chimene chimawononga, koma mugwilire ntchito chakudya chimene chimapatsa moyo osatha.”

-Kodi Yesu ankatanthawuza kuti ndikulakwa kugwira ntchito chifukwa cha chakudya?
-Ayi.

-Tonse tiyenera kugwira ntchito kuti tipeze chakudya.

-Kodi nanga Yesu ankatanthawuza chiyani?
-Yesu ankalankhula kuti ndikofunika kwambiri kuganiza za chakudya cha uzimu kusiyana ndi chakudya cha thupi.
-Yesu ankalankhula kuti ndikofunika kwambiri kugwilira nthito chakudya cha uzimu kusiyana ndi chakudya cha thupi.

-Kodi chakudya cha uzimu chimene ife tiyenera kuchigwilira ntchito ndi chiyani?
-Mawu a Mulungu.

-Kenako khamu la anthu lija linamufunsa funso Yesu.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:28-29

28-Chomcho iwo anamufunsa kuti, “Kodi ife tikuyenera kuchita chiyani kuti tichite tchito zimene akufuna Mulungu?”
29-Yesu anayankha kuti, “Chimene Mulungu akufuna kuti inu muchichite ndikukhulupilira mwa Iye amene anamutumizayo.”

-Kodi anthu anamufunsa chiyani Yesu?

-Anamufunsa kuti kodi ndi ntchito yanji imene iwo angagwire kuti amusangalatse Mulungu.



14-Anthuwo atachiwona chizindikiro chozizwitsachi anati, ”Zowonadi uyu ndiye Mneneri uja, amene malemba analankhula za Iye kuti adzabwera pa dziko la pansi!”
15-Apa Yesu anadziŵa kuti anthu aja ankafuna kuti amutenge momukakamiza kuti amulonge Ufumu, “chomcho Iye anachoka ndikupitanso ku phiri yekha.

-Kodi chifukwa chiyani anthu ankafuna kumupanga Yesu kukhala Mfumu?
-Chifukwa chakuti ankafuna kuti Iye adziŵapatsa chakudya nthaŵi iliyonse.

-Kodi anthu ankafuna kuti Yesu aŵapulumutse iwo ku tchimo, imfa ndi Satana?
-Ayi.
-Ankangoganiza za mimba zawo zokha.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanafune kuti akhale Mfumu ya anthu?
-Chifukwa chakuti Yesu anadziŵa kuti mitima ya anthu inali yoyipa.
-Chifukwa chakuti Yesu anadziŵa kuti anthu ankafuna kuti Iye adzingoŵapatsa chakudya basi.

-Chifukwa cha anthu, Yesu anapita kwayekha.

-Nthaŵi ya madzulo itafika, ophunzira a Yesu analoŵa mu ngalaŵa, ndipo anawuyamba ulendo owoloka nyanja ya Galileya.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:16-21

16-Dzuŵa litaloŵa, ophunzira a Yesu anatulukira ku nyanja,
17-anakwera mu ngalaŵa, ndipo ankawoloka nyanja kuloŵela ku Kaperenawo. Mdima unayamba, ndipo Yesu

anali asanadzebe kwa iwo.

18-Pa nthaŵi imeneyo mphepo ya mphamvu kwambiri inayamba kuwomba ndipo mafunde anayamba kukwera.

19-Ophunzira a Yesu aja anali atapalasa ngalaŵayo kwa mtunda wawutali pang'ono ndi pamene anamuwona Yesu akuyenda pamwamba pa madzi, akubwera moyandikira ngalaŵayo, ndipo iwo anawopa.

20-Yesu anaŵawuza kuti, "Musawope, ndi Ine!"

21-Kenako ankafuna kuti amutenge mu ngalaŵamo, ndipo mosachedwa ngalaŵayo inafika kumene ankapitako.

-Kodi chifukwa chiyani ophunzira a Yesu ankawopa?
-Chifukwa chakuti anamuwona Yesu akuyenda pa nyanja akubwera kwa iwo.

-Kodi pali munthu amene angathe kuyenda pa nyanja?
-Palibe.

-Yesu Yekha ndi amene anatha kuyenda pa nyanja.
-Palibe munthu wofanana ndi Yesu.

-Chifukwa chakuti Yesu ndi amene analenga nyanja, Iye anatha kuyenda pa nyanjapo.
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu, akhoza kupanga china chilichose chimene Iye wafuna.

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:22-25

22-Pa tsiku lotsatira lachelo, khamu la anthu limene linali kutsidya lina la nyanja, linadziŵa kuti kunali ngalaŵa imodzi yokha kumeneko. Iwo anadziŵanso kuti Yesu sanakwere pamodzi ndi ophunzira ache mu ngalaŵayo koma kuti iwo anadziŵa kuti ngalaŵayo inachoka mulibe Yesuyo.

23-Ngalaŵa zina zochokera ku Tibeliya, zinafika



kudzakocheza ku mtunda oyandikana ndi ku malo kumene linadyela mkate khamu la anthu lija Ambuye Yesu atayamika kwa Mulungu.

24-Khamu lija litawona kuti kunalibe Yesu kumeneko, ngakhale ophunzira ache, linakwera mu ngalaŵa ndikupita ku Kaperenawo kukamuyang'anayang'ana Iye.

25-Anthu aja atamupeza Yesu ku tsidya lina la Nyanja, anamufunsa kuti, "Mphunzitsi, munadza liti kuno?"

-Kodi chifukwa chiyani khamu la anthu linkamufunafuna Yesu?
-Chifukwa chakuti ankafuna kuti Iye aŵapatsenso chakudya china.

-Kodi Yesu ankachidziŵa chifukwa chimene ankamutsatilira Iye?
-Inde.

-Kodi Yesu analankhula chiyani kwa anthuwo?

Tiyeni tiŵerenga Yohane 6:26-27

26-Yesu anayankha kuti, " Ine ndikukuwuzani zowona kuti mukundifunafuna osakhala chifukwa chakuti munawona zizindikiro zanga zozizwitsa, koma chifukwa chakuti munadya mikate ndi kukhuta.

27-Musagwire ntchito kuti mupeze chakudya chimene chimawononga, koma mugwilire ntchito chakudya chopereka moyo osatha, chimene Mwana wa Munthu adzakupatseni. Ameneyo ndi amene Mulungu Atate anamulembera chizindikiro. "

-Yesu anaŵawuza anthuwo kuti iwowo amamufunafuna chifukwa chakuti anaŵapatsa chakudya.

-Kenako Yesu analankhula izi: